Mtengo wa feteleza m'Malawi muno ndi yokwera ndi makumi awiri and mphambu zisanu (25%) pazana limodzi (100) kuposa maiko olizungulira.

Ndipo boma linagawa timatumba ta feteleza ndi mbewu toyambira (starter pack) mchaka cha 1998 koma sitinakwani aliyese.

### **Fundo Zosonyeza Vuto Lomwe Lilipo Chifukwa Chakuti Mitengo Yogulira Mbeu Za Alimi Ndi Yostika Kwambi**

Mitengo ya fodya ina tsika ndi makumi anayi (40%) pa zana limodzi (100%) m'Malawi chaka cha 1998.

Malawi linalima fodya wokwana 90 miliyoni kilogalamu fodya wa bale mchaka cha 1998 mpaka 1999 kusiyana n fodya yemwe adali wo kwana 133 miliyoni kilogalamu. Kulingana ndi Bungwe lamalonda afodya la Toba Asosiyeshoni likosonyeza kuti alimi ali ngongole yo kwana K200 miliyoni Kwacha ku mabungwe angongole.

### **Fundo Yosonyeza Kuti Vuto Lomwe Lilipo Chifukwa Chakuti Mayendedwe Ndi Odula Zedi**

Mayendedwe akuno ku Malawi ndi odula kuposa aku Zimbabwe ndi Sosafrica ndi yoposa ndi kuchuluka ndi pak pochulukitsa ndi feri (3 times)

### **Fundo Zosonyeza Vuto Lomwe Lilipo Chifukwa Chakusowa Njira Zakasamalidwe Ka Bwino Ka Nthaka N Mbewu Zikupangitsa Kutha Chonde Mnthaka**

Alimi akugwiritsa feteleza wodula zedi kuti akolole zambiri chifukwa kudzala mbewu yomweyo chaka mcha kwapangitsa kuchotsa chakudya chachilengedwe munthaka ya m'Malawi muno.

Unduna wa zamalimidwe wunagawa fote kilogalamu tanzi ya feteleza chaka chaka 1998 mpaka 1999 ndipo fetele wochuluka akufunika mchaka chino cha 1999 mpaka 2000.

Mabungwe akunja akugwirira limodzi ndi mabungwe omwe si aboma kuno ku Malawi kuphunzitsa alimi akumud mmene angagwiritsire manyowa a chilengedwe kuti alowa mwa fetelza wopanga ku mafaiole.

### **Fundo Yosonyeza Vulo Lomwe Lilipo Chifukwa Chakuti Anthu Sakudziwa Mmene Angalimire Mbeu Zom Angagulitse Pa Mtengo Wo Kwera**

Mabungwe ambiri akugwira ntchito limodzi ndi alimi okwana makamu awiri (20%) pazana limodzi (100%) m'Mala muno powaphunzitsa kulima mbewu zina monga paprika, bowa ndi mbewu zina zomwe zingagulidwe pa mten wokwera.

### **Fundo Yosonyeza Vuto Lomwe Lilipo Chifukwa Chakuti Malo Omwe Adakagwiritsidwa Ntchi Yaulimisakugwiritsidwa Ntchito**

Bungwe losinthanso za kayendetsedwe ka malo oyenera kusunkha msokho pa malo omwe sakugwiritsid ntchito kuti zidzakhale zodula kwa eni ake ngati malo sakugwiritsidwa ntchito komabe akusunkhera msoko bule.

### 3. Maphunziro – Mavuto Ake

Ndivuto liti lomwe mukuganiza kuti ndivuti lenileni lamaphunziro m'Malawi. Nanga mphungu atati athane nalo vutolo athane ndi liti? Chongani kutsogolo kwa vuto lomwe mwasankha:-

- \_\_\_\_\_ Ana sangathe kupita kusukulu chifukwa sukulu zili patali patali kwambiri.
- \_\_\_\_\_ Ana sangathe kuphunzira chifukwa choti sukulu ndizowonongeka kwambiri.
- \_\_\_\_\_ Ana sangathe kuphunzira chifukwa chakusowa mabuku
- \_\_\_\_\_ Ana omwe ndi ophunzira msukuluzi amapita ndi njala ndipo chifukwa choti kulibe zopatsidwa chakudya cha masana cha sukulu
- \_\_\_\_\_ Aphunzitsi siokwanira mmasukulu
- \_\_\_\_\_ Aphunzitsi a sukulu za pulayimale sagwira bwino ntchito yawo
- \_\_\_\_\_ Sukulu siyiphunzitsidwa mchilankhulo chomwe ophunzira angachinvetse kapena kugwiritsa bwino ntchito.
- \_\_\_\_\_ Ana akusowa sukulu za sekondale chifukwa chokwera ntengo kwa sukuluzi
- \_\_\_\_\_ Zomwe ana amaphunzira ku sukulu za pulayimale sizingawathandize kuti azipeza nazo thandizo.
- \_\_\_\_\_ Zomwe ana omphunzira ku sukulu za sekondale amaphunzira sizi ngawathandize kupeza nazo thandizo atamaliza sukuluzi
- \_\_\_\_\_ Akuluakulu ndi ofunika kuti aphunzire kuwerenga ndi kulemba kuti adzitha ku lemba masamu

Mwasankha vuto limodzi lomwe ndi vuto lenileni lamaphunziro m'Malawi nanga mukuganiza kuti ndichifukwa chiyani vuto limeneli liri vuto lenileni?

---

---

Ganizani, mafunso awiri omwe mungafunse mphungu okhudza mavuto a mamphunziro.

Poyamba, ganizani za funso lokhudza zomwe mphunguyo adzachitepo pothetsa vutolo kunyumba.

---

---

Kachiwiri ganizani za funso lokhudza zomwe mphunguyo adzachitepo mogwilizana ndi anthu a mderalo pothetsa vutolo.

---

---

Aphungu ambiri amati adzathana ndi mavuto akhudza maphunziro. Funsani Phunguyo kuti nanga mungakhulupirere bwanji zoti iye adzathetsa vuto la mamphunzirolo.

---

---

## **Fundo Za Maphunziro**

Fundo zofotokoza vuto la sukulu za pulayimale kuti ndizotalikira kwa ana ena.

Ambiri ophunzira msukuluzi amayenda mtunda wokwanira makilomita asanu. Ndipo ophunzira amayenda kwa ora limodzi pa ulendo wawo wopita kusukulu komanso pobwerera ophunzira ambiri alibe nsapato.

## **Fundo Zosonyeza Kuwonongeka Kwa Sukuluzi**

Maperesenti makumi asanu ndi anai (90%) a ophunzira msukuluzi alibe nsapato. Maperesenti makumi asanu ndi anayi (90%) asukuluzi alibe madzi komanso zimbudzi.

Malawi akufunika makalsi osachepera 48, 433 kuti ophunzira amene alipo tsopano lino aphunzililemo. Maperesenti makumi asanu and awiri amaphunzilira panja chifukwa chosowa makalasi,

## **Fundo Zosonyeza Mulingo Wa Maphunziro**

Mchaka cha 1998 maperesenti khumi, asanu ndi limodzi (16%)ndi amane anakhoza mayeso a fomu foro ndiamene atalengeza pa zotsatira zamayesozi.

Kuperewera kwa amphunzitsi m'masukulu kwapangitsa kuti owona za maphunziro alembe anthu omwe siodziwabwino ntchito ya uphunzitsi kukakhala aphunzitsi. Mwa amphunzitsi 47, 370 mdziko lino la Malawi, amphunzitsi 24, 353 (51%) ali ndi zowayenereza zokwanira kuti akhaleli aphunzitsi.

Kuchepa kwa ndalama zamalipilo zamphunzitsi kumapangitsa kuti ophunzira asalimbikire kuphunzira kuti asadzakhale aphunzitsi. Choncho aphunzitsi ambiri amapita m'mapulayiveti sukulu pofuna malipiro abwino.

Fundo zokhudza vuto limene limapangitsa ophunzira mdziko muno kuti alephere kupita ku sukulu za sekondale.

Maperesenti asanu ndi limodzi (6%) a ophunzira sukulu za pulayimale ndi okhawo amane amapitiliza maphunziro awo kusukulu za sekondale.

## **Fundo Yosonyeza Vuto Kuti Ana Ambiri Sangapite Ku Sekondale Sukulu**

Maperesenti asanu ndi limodzi mwa ana a sukulu ndi amene amapita ku sukulu.

## **Fundo Zosonyeza Kuti Aphunzitsi Ndi Ochepe Komanso Osowa Kuti Apezeke Mdziko Muno**

Ophunzira ambiri mdziko muno amaphunzitsidwa popanda mlozo weniweniwamaphunziro (syllabus).

Mongoyerekeza chabe buku limodzi lowerenga pasukulu mdziko muno limagwiritsidwa ntchito ndi anthu asanu ndi awiri.

Mchaka cha 1995 msukulu za pulayimale mphunzitsi m'modzi amakhala ndi ophunzira 62. Pamene ku Zimbabwe ana ophunzira 44 amakhala ndi mphunzitsi m'modzi. Ndipo ku South Africa amakhala ophunzira 32 mphunzitsi m'modzi.

M'Malawi mpando umodzi umagwilitsidwa ntchito ndi ophunzira 48 ndipo tebulo limodazi limagwiritsidwa ntchito ndi ophunzira 38 msukulu za pulayimale.

## **Mfundo Zosonyeza Kuti Zimene Ophunzira Anaphunzira Msukuluzi Sinzi Ngawathandize Kupezanazo Tsogolo La Bwino**

Maphunziro ambiri monga, chisamaliro cha pakhomo, ukalipentalandi ntchito za manja akuchotsedwa msukulu kamba kosowa zinthu zofunika kugwilitsidwa ntchito m'mphunzirowa.

## **Fundo Zosonyeza Kuti Akulu Ambiri Mdziko Muno Akufunika Kuti Aphunzitsidwe**

Maperesenti 55 a nthu omwe ndi a kuluakulu ndi omwe amatha kuwerenga ndipo maperesenti 42 azimayi ndi okhawo omwe amtha kuwerenga mdziko muno.

#### 4. Miseu, Ulalo, Madzi Ndi Mtokoma

Madzi liti lokhudza miseu, ulalo madzi kapena mtokoma ndziko lino la Malawi. Lawonongeka kwambiri. Nanga mphungu atafuka kuchitapo kanthu athane ndi liti? Chongani vuto imodzi lomwe mwasankha lokhudza miseu, ulalo, madzi kapena mtokoma:-

- \_\_\_\_\_ Midzi yina yilibe miseu yopita kumalo ochitilako malonda.
- \_\_\_\_\_ Miseu ya m'midzi ndi yozungulira midziyo ndiyowonongeka kwambiri
- \_\_\_\_\_ Ulalo ufunika kuti ukonzedwepena kumangidwa ya tsopano.
- \_\_\_\_\_ Miseu ya mmizinda ndi yozungu lira mizinda ndi yapakati pa mizina ndi yowonogeka.
- \_\_\_\_\_ Anthu amayenda mitunda italiitali kuti apeze madzi ndipo akawa peza madziwo ayenera kuyamba awawilitsanso kaye kuti amwe.
- \_\_\_\_\_ Anthu amlephera kupeza madzi ngakhale ayende mitunda italiitali.
- \_\_\_\_\_ Magetsi sakupezeka mmadera ambiri
- \_\_\_\_\_ Lamya zam'madera sizipezeka pafupi ndipo ndi zowonongeka.
- \_\_\_\_\_ Wailesi sipereka uthenga wofunikira kwa anthu.
- \_\_\_\_\_ Kuchepa kwa mphavu za wailesi

Mwasankha umodzi mwa nseu, ulalo, madzi kapena mtokoma omwe ndivuto m'Malawi . Nanga mukuganiza kuti nchifukwa chiani limenero liri vuto lenileni.

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

Ganizani mafunso awiri omwe munga funse phungu okhudza za vutolo.

Poyamba ganizani za funso lomwe likukhudza zomwe mphungu achitepo pofuna kuthetsa vutolo ku nyamba yamalamulo.

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

Kachiwiri ganizani za funso lomwe likukhudza zomwe mphunguyochite mogwirizana ndi anthu a mderalo pothana ndi vutolo.

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

Amphungu ambiri anati adzathana ndi vuto la miseu, ulalo, madzi ndi mtokoma funsani mphunguyo kuti nanga inu mungakhulupirile bwanji zoti iye adzathana nawo mavutowo.

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

### **Fundo Zosonyeza Mavuto Alipo Chifukwa Chakusowa Matelefoni (Lamya)**

Poyerekeza m'Malawi ndi miako ena pa nkhani ya matelefoni (lamya) ku kenya tikulowamo kawiri pakuchuluka kwa telefoni, ndipo ku Zambia tikulowamo ka wiri ndi theka pa kuchuluka kwa telephone m'Malawi muno.

Pali anthu 25, 000 omwe akudikirira kuti awayikira ma telefoni nyumba zawo m'Malawi muno.

Panja (Public Phone) ya anthu limodzi pa anthu 22, 000 aliwonse m'Malawi muno. Ndipo Bungwe lowona za matelefoni M.P.T.C. m'Malawi muno lili ndi chiyembekezo chakuti liyike telefoni ya panja ya pabuliki limodzi pa anthu aliwonse okwana 2000 pofika chaka cha 2000.

### **Fundo Yosonyeza Vuto Lomwe Lilipo Chifukwa Cha Kusowa Kwa Magetsi**

Pazana limodzi pali anthu atatuakumudzi omwe ali ndi mwayi okhala ndi magetsi. Ndipo maiko ozungulira ali ndi mwayi okhala ndi magetsi.

### **Zomanga Manga - Fundo Ndichidziwitso**

#### **Fundo Zosonyeza Mavuto Omwe Alipo Ndi Miseu Ndi Milato**

Pali 14, 500 kilomitazi (Km) ya misewu m'Malawi ndipo miseu yochepa zedi ndi yoyika mphula, pa miseu yo kwana zana (100%) pali miseu yokwana makumi awiri (20%) yoyika phula.

Mchaka cha 1996 theka chabe ya miseuyi inali yodutsa.

Bungwe la MASAFU, pabuliki wekisi linali ndi mapulojeketi 379 wokhudza za misewu ndi za kasungidwe ka madzi.

#### **Fundo Zosonyeza Mavuto Omwe Alipo Chifukwa Cha Madzi Osatetezedwa**

Mchaka cha 1995 anthu 45 pa anthu za limodzi (100) lililonse anali ndi madzi otetezedwa m'Malawi muno.

Zaka zingapo theka ya ana a m'Malawi muno analandira makhwala aja owonjezera madzi mthupi. Ichi ndi chithandizo chomwe chikuperekedwa kwa ana kawirikawiri chifukwa cha kuchepa kwa unkhondo pa nyumbamwinanso chifukwa cha kuchepa kwa ana kawiri kawiri chifukwa cha kuchepa kwa unkhondo pa nyumba mwinanso chifukwa chakusowa madzi abwino otetezedwa ndipo pa zana limodzi (100%) pali anthu okwana makumi asanu ndi anayi (93%) omwe amagwiritsa ntchito nkhu ni pa zonse zawo zokhudza moto.

#### **Fundo Zosonyeza Vuto Lomwe Lilipo Chifukwa Chosakhala Ndi Zidziwitso/Mauthengo Othandiza Pa Wayilesi**

Nthawi yochepa zedi pa wayilesi ya 1 ndi 2 (kuchepa 5%) ndi imene linagwiritsidwa ntchito kuphunzitsa zinthu zofunika kufuko la Malawi.

## 5. Chisamaliro Cha Umoyo

Ndivuto liti lomwe mukuganiza kuti ndiro vuto lenileni lokhodza za chisamiro cha umoyo? Nanga mphungu atati athane nalo vuto athane ndi litiro? Chongani vuto limodzi lokha lomwe mwasankha:-

\_\_\_\_\_ Zipatala zambiri zili kutali ndi midzi ndiye anthu sangathe kuyenda pansu kupita kuzipatalazo

\_\_\_\_\_ Zipatala zambiri zilibe mankhwala ndizofunikira zina.

\_\_\_\_\_ Akulu onse amuna kapena akazi akufunika kumphunzitsidwa za matenda a Adzi ndi mapewedwe ake.

\_\_\_\_\_ Anyamata ndi atsikana ndiofunika kuwaphunzitsa za Adzi ndi mapewedwe ake.

\_\_\_\_\_ Makondomu apatsidwe kwa anthu ulere kapena agulitsidwe pantengo wotsika kwambiri kwa aliyense amene akufuna kondomuyo.

\_\_\_\_\_ Maphunziro okhucha kudwala kupewa matenda omwe anga bwere chifukwa chopanda ukhondo wabwino.

Mwasankha vito la za umoyo limodzi lomwe mukuganiza kuti ndi vuto lenileni m'malawi muno. Nanga nchifukwa chiya ni mwasankha vuto limenelo?

---

---

Ganizani za mafunso awiri omwe munga funse phungu okhudza vitolo

Poyamba funsani za funso lomwe likukhudza zomwe mphungu adzapange pothetsa vitolo akapita kunyumbaya malamulo.

---

---

Kachiwiri ganizani za funso lomwe likukhudza zomwe mphunguyo mogwirizana ndi anthu amderalo adzapange pofuna kuthetsa vitolo.

---

---

Ampungu ambiri amati adzathetsa mavuto a zaumoyo. Funsani kuti nanga inu mungakhulipirire bwanji zoti adzathetsadi mavutowo

---

---

## **Mbiri Ndi Fundo Za Umoyo**

### **Fundo Zosonyeza Kuti Madotolo, Anamwino Ndi Zipatala Zing'onozing'ono Ndi Zoperewera**

Malingana ndi ndodomeko ya bungwe lowona za umoyo padziko lonse la pansi (WHO) payenera kukhala dotolo m'modzi kwa anthu 10, 000 ali wonse, Mnamwino m'modzi kwa anthu 1, 000 aliwonse ndipo lwa odwala mano 1, 000 ayenera kuthandizidwa ndi wamano m'modzi. Koma m'Malawi anthu 81, 000 amakhala ndi dotolo m'modzi, anthu 19, 500 amakhala ndi namwino m'modzi ndi anthu 1, 900 000 odwala mano amakhala ndi dotolo wa mano m'modzi basi.

Pali mipando 113 ya a dotolo akuluakulu m'Malawi koma mipando 72 yokha ndiyo iri ndi anthu. Ndipo pali mipando 380 anamwino (Nurses) 74 yokha ndiyo iri ndi anthu, ndipo pali mipando 1549 anamwino (Widwives) 1270 yokha ndiyo iri ndi anthuwu.

Maperesenti 30 okha a anthu a m'midzi ndiwo odziwa bwino zaumoyo wa bwino.

### **Fundo Zosonyezamavuto Okhudza Matenda A Edzi Ndi Tizilombo Ta Hiv**

Chiyembekezo cha moyo m'Malawi chinayenera kukwera kuchokera pa zak 45.2 mchaka cha 1997 kufika pa 57 pofika chaka cha 2010. Koma chifukwa cha matenda a Edzi moyo ukuyembekezeka kukwera ndi zaka 34 zokha pofika 2010.

Pafupifupi maperesenti 15 a chiwerengero cha anthu mmalawi ali ndi tizilombo ta HIV. Ndi akazi maperesenti 30 ali ndi tizilombo ta HIV mu mzinda wa Lilongwe ndi Blantyre

Pofika mchaka cha 2005 imfa idza kwera ndi maperesenti 80 – 85% mu mzinda wa Lilongwe, Blantyre ndi Mzuzu chifukwa cha matenda a edzi

Mdziko la Malawi atsikana a zaka 15 ndi 19 pa adzatenga amatendawa kuposa anyamata ndi kasanu (5 times) omwe ali ndi zaka zomwezi.

Mabuungwe oteteza matenda a edzi ndi tizilombo ta HIV kuti isafalikire analandira ndalama zokwanira 25 miliyoni ndalama za kwa Amerika (US\$ 25, 000, 000) mchaka cha 1996. Kufikira mchaka cha 1999. Ndondomekoyi yilindizolinga izi:-

- Kuteteza matenda a edzi pa gulu la anthu okhala pa malo amodzi
- Kukhala ndi maphanziro okhudza chitetezo ku matendawa a edzi
- Kukweza njira zo gawira makondomu
- Masamalidwe a anthu omwe ali ndi tizilombo ta HIV mmanyumba mwawo
- Kukweza njira za chisamaliro cha umoyo wa ana omwe ali ndi tizilomboti, ndi achinyamata ndi mabanjanso.
- Kukweza njira zokhudza umoyo wa amuna ndi akazi mofanana.

### **Fundo Zofotokoza Kusowa Kwa Maphunziro Okwanira Pa Za Ukhondo**

Theka la ana a mdiko muno zaka zapita zo amalandira madzi anthupi iyi ndi njira imodzi yosavuta pakuteteza matenda omwe amabwera chifukwa cha vuto la ukhondo. (Kusasamala)

## 6. Ziwawa Ndi Chitetezo Cha Munthu

Ndivuto liti lomwe mukuganiza kuti ndilo limabweretsa chisokonezo kwambiri m,malawi? Nanga Mphungu atafuna kuchitapo kanthu angathane ndi vuto litilo poyamba? Chongani kutsogolo kwa vuto lomwe mwasankha:-

- \_\_\_\_\_ Achinyamata ayenera kuphunzitsidwa kulemekeza anthu ena ndi zinthu zawo.
- \_\_\_\_\_ Anthu akamangidwa chifukwa cha mlandu woyanbitsa chisokonezo asamatulutsidwe asanaweluzidwe
- \_\_\_\_\_ Anthu m'mudzi ndi mmadera awo ayenera kukhala odalilana kuti apewe ziwawa pokhala aliyense mulonda wa mzake.
- \_\_\_\_\_ Anthu akufunika kuti aphunzitsidwe kuti asamapeleke chilango okha kwa zigawenga mmalo mwakeadzipereka anthuwu kwa ulamuliro woyenera kuti achitepo kanthu
- \_\_\_\_\_ Apolisi ayenera kuchitapo kanthu msanga akawuzidwa za ziwawa

Mwasankha vuto limodzi lomwe ndi vuto lalikulu lokhudza ciwawa m'malawi. Nanga nchifukwa chiani mulikuganiza kuti vuto limenero ndiro lenileni.

Ganizani mafunso awiri omwe munga funse Phungu okhudza za vutoli

Poyamba ganizani za funso lomwe mungafunse mphungu lokhudza zomwe mphunguyo adzachitepo pothana ndi vutolo.

---

Kachiwiri ganizani za funso lokhudza zomwe mphunguyo mogwilizana ndi anthu amderalo adzachitepo pothetsa vutolo.

---

Aphungu ambiri amati adzathana ndi mavuto aziwawa. Funsani mphungu yo kuti nanga munga khulupilire bwanji kuti adzathana nawo mavutowo.

---

---



### **Fundo Ndi Mbiri Yokhudza Chitetezo Cha Anthu**

Fundo zosonyeza kuti achinyamata ayenera kuphunzitsidwa zolemekeza anthu ena ndi zinthu zawo.

Mbala ndi zigawenga zambiri m'Malawi muno ndi amuna a zaka 15 kufikira 30.

### **Fundo Zokhudza Kumasulidwa Kwa Mbala Ndi Zigawenga Pa Belo**

Malamulo a m'Malawi muno amati munthu akamangidwa ayenera kutuluka pakatha masiku awiri. Mbala ndi zigawenga zambiri zimamasuludwa zikangoweluzidwa. Ndende zilibe malo okwanira osungira anthu amane aweruzindwa ndipo opezeka olakwa. Mwa akayidi 6800 m'ndende za Malawi maperesenti makumi atato (30%) amasungidwa podikirira tsiku la mlandu wawo.

Mbala ndi zigawenga zambiri zika tuluka pa belo sizimabwereranso kuti zikanve zotsatila. Ambiri amati akatero amangwindwanso nazengedwa mulando wapoyamba komanso mlandu wosatsata malamulo a belo.

Pali anthu a ndende oposa 5000 m'Malawi.

Malingana ndi wankulu wa malamulo m'Malawi wati akayidi amalandira theka la chakudya chimene ayenera kulandira pa tsiku izi ziri choncho chifukwa choti ndalama zogwiritsira ntchitoyi ndizoperewera ku maperesenti 25 a ndalam zofunikira.

### **Fundo Zokhundza Chitukuko Ndi Chitetezo Cham'madera Ku Ziwawa**

M'maboma apolisi akhazikitsa magulu achitetezo 16 a m'madera. Ndongomekoyi yikuphunzitsa anthu omwe ndi mzika za dziko lino momwe angadzitetezere komanso momwe angayambire kudalirana kwa wina ndi mzache pachitetezo cham'makomo.

### **Fundo Zokhudza Chilango Chomwe Anthu Amapatsa Wolakwila Potsata Ndongomeko Ya Ulamuliro Wochokera Kwa Olamulira**

Kuzunza ndi kutentha wolakwira, ndi chiwawa m'Malawi. Apolisi amakhulupilira kuti izi ziyambitsa chisokonezo.

M'malo moteteza chisokonezo. Apolisi amakhulupilira kuti chenicheni chomwe chimayambitsa nchitidwe woyatsana ndi kusanvetsa bwino za kutuluka pa belo.

Apolosi amakhulupilira kuti chilango cha ndende chidzikhalira mbala ndi zigawenga zowopsya ndipo milandu yaying'onoing'ono idzi weruzidwa m'madera mwa anthu momo.

Apolisi akuno ku Malawi akuwona kuti chiweruzo chopita ku ndende chikhalire olakwa zedi ndipo a milandu yaying'onoying'ono azigwira ntchito ya m'madera.

### **Fundo Zomwe Zimawalepheretsa Apolisi Kuchitapo Kanthu Nsanga Akafunidwa**

Pali aPolisi 6000 m'Malawi m'malo mwa apolisi 24000

Apolisi amakhulupirira kuti pakufunika maphunziro okwanira pa zofufuza a zinthu ndi kukhala ndi mayendedwe okwanira

## 7. Ntchito Za Malonda Ndi Ntchito Zina

Ndivuto liti lomwe mukuganiza kuti ndivuto lokhudza kwambiri ntchito za malonda ndi ntchito zina m'Malawi? Nanga mphungu atafuna kuti athane ndi vuto limodzi lokhudza ntchito za malonda ndi nchito zina athane ndi litiro? Chongani vuto limodzi lokha lomwe mwasankha:-

\_\_\_\_\_ Anthu akusowekera maphunziro okhudza mayambidwe ndi mayendatsedwe a mabizinesi ang'onoang'ono

\_\_\_\_\_ Njira yopatsa anthu ndalama zoyambira bizinesi pangongole zipezeke.

\_\_\_\_\_ Boma lipezere ntchito anthu osauka omwe sangathe kugula kapena kulima chakudya okha ndipo boma lidziwalipira anthuwo chakudya.

\_\_\_\_\_ Njira zoyendetsera katundu wa anthu amabizinesi ang'onoang'ono kupita naye ku misika ndi zofunika kuti zipezeke.

\_\_\_\_\_ Anthu akufunika maphunziro omwe angawathandize kuti apeze ntchito.

Mwasankha vuto limodzi lomwe ndilokhudza ntchito za malonda ndi ntchito zina m'Malawi. Nanga nchifukwa chiyani mukuganiza kuti limenelo ndiye vuto lenileni

Ganizani mafunso awiri omwe mungafunse phungu okhudza za vutoli.

Poyamba ganizani za funso lomwe likukhudza zomwe phunguyo adzachitepo pofuna kuthetsa vutolo akapita ku Nyumba ya Malamulo

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

Kachiwiri ganizani za funso lomwe likukhudza zomwe mphunguyo mogwilizana ndi anthu a mderalo adzachite pofuna kuthetsa vutolo.

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

Aphungu ambiri amanena kuti adzathana ndi mavuto okhudza ntchito zamalonda ndi ntchito zina. Funsani mphungu wanu kuti nanga inu mungakhulupilire bwanji kuti iye adzachitapo kanthu.

## **FUNDO NDI MBIRI YA ZA MALONDA NDI NTCHITO**

### **FUNDO ZA KUSONYEZA KUSOWA KWA CHITUKUKO MUNTCHITO NDI MALONDA**

Malinga ndi kafukufuku wamalipiro a anthu m'Malawi pa mapeto pa mwezi munthu amalandira MK1,800.00.

Malingana ndi banki yayikulu pa dziko lonse ya (World Bank) malipiro a munthu wogwira ntchito ku mafikitare anatsika kuchokera pa 55 ndalama za ku America kufika pa 13 m'chaka cha 1996.

Monga mwa banki lalikulu pa dziko lonse chuma cha Malawi chimayenera kuti chikwere ndi mapersenti 5 kapena 6 pa chaka poteteza umphawi kuti usafike poyipa. Komanso zinthu zopangidwa mdziko momuno (Mlingo umodzi wa chuma GDP) chakwera ndi mlingo wa maperesenti atatu ndi theka pa chaka kuchokera mchaka cha 1990.

Mlingo wa GDP mdziko muno ndi 220 ndalama za ku America. Mlingowu ndi wochepera ku mlingo wa theka waku sahara mu Africa.

## 8. Ufulu Wa Amayi Ndi Ana

Ndivuto liti lomwe mukuganiza kuti ndilokhudza amayi ndi ana kwambiri m'Malawi? Nanga mphungu atati achitepo kanthu mukuganiza kuti athane ndi vito limodzi lokha lokhudza amayi kupena ana okha.

\_\_\_\_\_ Atsikana samasamalidwa bwino mofanana ndi anyamata m'sukulu.

\_\_\_\_\_ Amuna amamenya akazi awo koma salangidwa chifukwa chakumenya akazi awowo

\_\_\_\_\_ Atsikana ndi amayi amachitidwa chipongwe powagwililira ndikuchita nawo zachiwerewere ndi amuna koma amunawo salandila chilango.

\_\_\_\_\_ Katundu wa anafedwa amalandidwa ngakhale zili zotsutsana ndi malamulo.

\_\_\_\_\_ Azimayi sanvetsa za ufulu wawo kotero kuti satha kuyima okha chifukwa chamantha.

\_\_\_\_\_ Amuna amagona ndi azimayi ambiri ndipo salola kuteteza akazi awo ku Edzi pogwilitsa ntchito kondomu.

\_\_\_\_\_ Mabanja akulephera kusamala ana amasiye.

\_\_\_\_\_ Ngakhale kuti ndikulakwira malamulo kulanda chuma cha akazi amuna awo atamwalira anthu ambiri amalandabe azimayi katundu wawo.

Mwasankha vuto limodzi lomwe ndi lokhudza amayi kapena ana kwambiri a mdziko lino la Malawi. Nanga ndi chifukwa chani inuyo mwasankha vuto limenelo.

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

Ganizani mafunso awiri omwe mungafunse mphungu wanu okhudza za vutoli.

Poyamba ganizani za funso lomwe ndilokhudza zomwe mphunguyo adzachitepo pothetsa vutolo akapita ku Nyumba ya Malamulo.

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

Kachiwiri ganizani za funso lomwe ndilokhudza zomwe mphunguyo mogwirizana ndi anthu amdera lake adzachitepo pofuna kuthetsa vutoli.

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

Amphungu ambiri amati adzachitapo kanthu pofuna kuthetsa vuto lokhudza amayi ndi ana. Funsani mphunguyo kuti nanga mungakhulupilire bwanji kuti iyeyo adzachitapo kanthu.

### **Mbiri Ndi Fundo Ya Ufulu Wa Amayi Ndi Ana**

Fundo yosonyeza kuperewera kwa khumbo la amayi m'maudindo akuluakulu.

Mwa aphungu anyumba yamalamulo 177 aphungu 9 okha anali amayi. Nduna za boma 20 nduna ziwiri zokha zinali amayi panopa.

Amayi ochepera maperesenti asanu (5%) okha omwe amagwira ntchito kumalo anrchito ena osati pakhomo ndiwo amagwira ntchito za dongosolo la ntchito ndi ubwana.

### **Fundo Yosonyeza Vuto La Atsikana M'maphunziro Ndi M'machitachita Ena**

Mchaka cha 1995 atsikan maperesenti awiri okha ndiwo anali ndi mwayi ophunzira msikulu za sekondale. Kufanizira ku maperesenti 9 anyamata

Mdera la mfumu Tsabango muli ma bungwe a chinyamata 32 ndi mamembala alipo 1100 koma ndi maperesenti 25 okha omwe ndi atsikana.

### **Fundo Yosonyeza Vuto Logwilitsa Ntchito Ana**

Monga mwa banki lalikulu pa dziko lonse theka la mthekero wa theka la chowerengero cha ana ochepera zaka khumi ndi zinayi (14) amagwira nchito kunjira kwa mabanja awo.

## 9. Ziphuphu

Ndivuto liti lomwe mukuganiza kuti ndi vuto lomwe lafika pamponda chimera muziphuphu m'Malawi? Nanga mphungu atafuna kuchitapo kanthu ayambe ndikuthana ndi vuto liti pa ziphuphu? Chongani vuto limodzi lomwe mwasankha.

\_\_\_\_\_ Akuluakulu a boma amagwilitsa ntchito maudindo awo kuti alemere

\_\_\_\_\_ Aphungu a Nyumba ya Malamulo anagwilitsa ntchito maudindo awo kuti alemere.

\_\_\_\_\_ Akulu akulu a boma sasamalira anthu azipani zosiyanasiyana mofunana.

\_\_\_\_\_ Mafumu amakondera chipani chimene iwo akuchikonda ndikupondeleza zipani zina.

\_\_\_\_\_ Amalonda sapeleka ndalama zamsonkho zomwe ayenera kupeleka.

Mwasankha vuto limodzi lomwe ndi lopera mavuto onse aziphuphu m'Malawi nanga ndifukwa chani mwasankha vuto limeneli?

\_\_\_\_\_

Ganizani mafunso awiri omwe mungafunse mphungu wanu okhudza za vutoli

Poyamba ganizani za funso lomwe ndilokhudza zomwe mphunguyo achite pofuna kuthana ndivutolo akapita ku Nyumba ya Malamulo

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

Kachiwiri ganizani za funso lomwe ndilokudza zomwe mphungu yo mogwilizana ndi anthu a mdera lakero adzachitepo pofuna kuti athane ndi vutolo.

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

Aphungu ambiri amati adzathana ndi mavuto okudza ziphuphu. Funsani kuti nanga inu mungakhulupilire bwanji kuti iye adzachitapo kanthu pa vutoli

## **Fundo Ndi Mbiri Ya Ziphuphu**

### **Fundo zosonyeza ziphuphu**

Kuyambira pamene bungwe lowona ndikuthetsa za ziphuphu linyamba ntchito zake mchaka cha 1996 latha kuperekako ripoti lapachaka kamodzokokha lokhudza ntchito yawo. Malingana ndi lamulo la nchitidwe waziphuphu limene linakhazikitsidwa mchaka cha 1995, akulu oyimira zochitika mdziko lino (National Assembly) ayenera kuliwona bwino lipotili ndipo ayenera kuchita ndemanga yokhudza momwe iwo ayiwonwera ngati nkwabwino kutero. Kufikira lero lipotili silinakambidwebe pakati pa aphungu muyumba yamalamulo.

Chaka cha 1998 bungwe lowona za ziphuphu ndi kuthetsali lina landira makalata kuchokera kwa theka la anthu okhala mmalawi, ndipo analandimalipo 500 ochokera kwa akuluakulu ena okhudza ziphuphu. Mchaka cha 1998 bungwe lowona ndikuthetsa ziphuphu anathana ndi mavuto okhudza ziphuphu akulu zo ndipo panopa pali mavuto ena 180 amene akanafufuzidwabe. Bungweli lathana ndi milandu itatu ndipo milandu yina 5 ikudikira kuti athanenayo.

## 10. Chithandizo Chochokeza Kunja, Chuma Cha Mbanki Akunja Ndi Malonda

Nanga ndi vuto liti lomwe mukuganiza kuti ndi vuto lomwe lafika poyipitsitsa lokhudza chithandizo chochokera kunja ndi mmabungwe, chithandizo chochokera kunja ndi malonda m'Malawi? Nanga mphungu atati athane ndi limodzi athane ndilitiro? Chongani vuto lomwe mwasankha, limodzi lokha basi:-

\_\_\_\_\_ Amalonda akusowa kuphuzitsidwa momwe angapititsire patsogolo katundu wawo kuti azimugulitsa pantenga wotsika kusiyana ndi katundu wochokera kunja.

\_\_\_\_\_ Miseu, mayendedwe, mphanvu yamagetsi ndi lamya ziyenera kuti zitukuke ndikupita patsogolo kuti anthu akhale ofuna kuyamba zamalonda mumabizinesi awo m'Malawi.

\_\_\_\_\_ Mayiko ndi mabungwe omwe amathandiza dziko la Malawi pa chuma akhululukire Malawi ngongole zache kotero kuti Malawi asamagwilitse ntchito ndalama zambiri pofuna kubweza ngongolezo

\_\_\_\_\_ Maphunziro ndikuphunzitsa anthu za ntchito ziyenera kupita pa tsogolo kuti anthu adzayambitsa mabizinesi awo adzipeza anthu otha ntchito yawo bwino m'Malawi momuno

Mwasankha vuto limodzi lokhudza mayiko ndi mabungwe omwe amathandiza dziko lino, chuma chamayiko ena kapena malonda omwe ndivuto lenileni la m'Malawi. Nanga ndichifukwa chani mwasankha vuto limenero.

\_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_  
Ganizani mafunso awiri omwe mungafunse mphungu wanu okhudza za vutoli

\_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_  
Poyamba ganizani za funso lomwe ndilokhudza zomwe mphungu akapita ku Nyumba ya Malamulo adzachitepo pofuna kunthana ndi vutolo.

\_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_  
Kachiwiri ganizani za funso lomwe ndi lokhudza zomwe mphunguyo mogwilizana ndi anthu a mdera lake adzachitepo pofuna kuthana ndi vutolo .

\_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_  
Amphungu ambiri anati adzathana ndi vuto lokhudza chithandizo kuchokera mmaiko ndimabungwe, chuma cha maiko ena komanso malonda, funsani mphungu kuti nanga inu mungakhulupilire bwanji kuti iye adzathandiza



### **Fundo Ndi Mbiri Ya Chithandizo Chochokera Maiko Ena Chuma Chokhala Mmabanki Akunja Ndi Zamalonda**

Fundo yofotokoza za vuto lokhudza kuyitanitsa katundu wochuluka kuchokera mmaiko akunja ndikutumiza katundu kunjwa wochepe

Mchaka cha 1997 malawi anagulitsa kutundu ku maiko a kunjwa wokwanira MK236.9 milliyoni ndipo anagula katuindu wochokera kunjwa wokwana MK 700 miliyoni.

### **Fundo Yokhudza Misika Yikuluyikulu Mdziko Lapansi**

Owona za chuma cha maiko pa dziko lonse lapansi ndi a bungwe lokhudza zofufuza chuma ndi misika yodziwika bwino lotchewa "Harvard Group" linayika dziko la Malawi pa nambala 23 pamaiko a mu Africa amene anawapeza kuti ali ndi misiko yayikulu mmalonda a pa maiko.

### **Fundo Yokhudza Chithandizo Chochokera Kunja**

Mchaka cha 1996 Malawi analandila thandizo lochokera kunjwa lokwana USD 501 miliyoni ndalama za ku Amerika

### **Fundo Lokhudza Ngongole Zamaiko**

Malawi ali ndi ndalama zokwanira madola a ku Amerika 2.4 billiyoni za bungwe la "International Community" pa ngongole zake dzikolo limayenra kuma pereka maperesent (25%) ya ndalama zomwe dzikolo lapeza pogulitsa kutundu wake mmaiko ena koma dziko la Malawi lima gwilirtsa ntchito maperesenti 17 okha a ndalama zomwe linapeza pogulitsa katundu wake kunjwa kwa dzikoli pofuna kubweza ngongole zake

Banki lalikulu pa dziko lonse la "World Bank" likubwereka Malawi ndalama zokwanira madola aku Amerika 92 milliyoni (MK 4.05 billiyoni) kuboma la malawi ziti ligwilitse ntchito pa chitetezo.

## Briefing Book Bibliography

*ACB News, Bi-Monthly Newsletter of the Anti-Corruption Bureau*, Vol.1, No. 6

Article XIX, interview with Robert Jamieson

*The Binoculars* (newspaper), "Seminar 'wakes up' girls to gender issues", November 16-22, 1998

*The Daily Times* (newspaper), "Agriculture slumps in 1998", December 3, 1998, "Poor results due to lack of syllabus – association", March 8, 1999, "Committee campaigns for Malawi's debt relief", March 18, 1999

Danish Ministry of Foreign Affairs, "MALAWI Strategy for Danish – Malawi Development Cooperation"

*The Eagle, The Magazine for the Malawi Police Service*, Vol.25, No.2

*The Enquirer* (newspaper), "UDF fulfils manifesto pledge on agriculture", March 10, 1999

European Commission Office for Food Security, interview with Maryliza Santo-Nocito

European Community, Malawi Office, "Customary Land Use Study, 1998", Executive Summary

European Community, Malawi Office, "Malawi: Review of Food Security Information Systems"; number 1, March 1999

European Community, Malawi Office, "Malawi: Structure of Fertiliser & Transport Costs"; number 3, April 1999

Government of Malawi, Malawi Police Service, interviews with Oliver Soko, Press and Public Relations Officer, and Elvis Thodi, Senior Assistant Commissioner of Police

Government of Malawi, Ministry of Education, "PIF 1999: Basic Education Status Report" (draft)

*The Hansard of the National Assembly of Malawi*

International Monetary Fund, "Malawi – Enhancement Structural Adjustment Facility Policy Framework Paper, 1998/99 – 2000/01"

*The Lamp*, (magazine) "Malawi Debt Cancellation Campaign", "The Earnings of the Poor: Should They Be Taxed", March-April 1999

Malawi Agro-Forestry Project, interviews with Glynwel Siyeni and M. Mpira, Technical Associates

Malawi National Commission for United Nations Educational Social and Cultural Organization (UNESCO), interviews with Hyacinth Kishindo and David Mulera

*The MASAF Factfile*, Malawi Social Action Fund, January 1999

*The Nation* (newspaper), "Bumper yields expected", February 24, 1999, "Women deplore property seizure", October 19, 1998, "Speed up land distribution", December 7, 1998, "IDA

approves K4.05bn", December 24, 1998, "Starter pack promises high yields", February 18, 1999, "Prisoners on half meals till June", April 14, 1999, "Why investors shun Malawi", December 23, 1998

Pan African News Agency, "Malawi Predicts Low Tobacco Yield", April 7, 1999

Save the Children USA, Malawi Field Office, "The Cope II Program, Executive Summary"

Save the Children USA, interview with David Chilongozi, Senior Program Manager, Malawi Field Office

United Nations Development Programme, "Human Development Report 1998"

United Nations, AIDS Project, "The Readiness of Malawi for an Intensified Response to HIV/AIDS" (draft)

United States Agency for International Development, "Malawi and HIV/AIDS"

United States Department of State, "The 1998 U.S. Department of State Country Human Rights Report, Malawi"

World Food Programme, interview with Kenton Kayira, National Programme Officer

World Bank, "African Development Indicators, 1998/99"

World Bank, "Safety Nets Presentation", Jim Smith, Deputy Resident Representative, Malawi

